Centre for Environmental Policy and Advocacy

July 2021
Vol. 19. Issue 1.

# KUPHIKA MWAMAKONO KUTI NKHALANGO ZATHU ZITETEZEKE



Mphamvu za magetsi zimatithandiza kugwira ntchito zosiyanasiyana, monga kuphikira, kuwalitsira m'chipinda kapena pamalo, kutenthetsera zinthu, komanso kuyendetsa ntchito za mafakitale.

- Amalawi ambiri sagwiritsa ntchito magetsi opangidwa kuchokera kumphamvu za madzi, dzuwa kapena mphepo.
- Mapeto ake, anthu amagwiritsa ntchito nkhuni kapena makala osavomelezeka pophika komanso kutenthetsa zinthu. Muchitidwewu ukupangitsa  kuti nkhalango zathu zizipululuka mwachangu.
- Mitengo ikagwetsedwa, nthaka imakhala yosatetezeka ku mvula ya mphamvu. Zimenezi zimapangitsa kuti nthaka ya chonde nayo ikokokoloke ndi kuika anthu pa chiopsezo cha njala popeza mbewu sizimera bwino.
- Mchitidwe odula mitengo wapangitsanso kuti matope adzikokoloka ndi madzi ku mtunda, ndi kukasokoneza ntchito yopanga magetsi odalira mphamvu ya madzi mu mtsinje wa Shire. Mapeto ake, anthu ogwiritsa ntchito magetsi amagula magetsiwo pamtengo okwera, zimene zikupangitsa kuti makala aziyenda malonda.
- Nkhani yabwino ndi yokuti pali njira zabwino zopezera mphamvu za magetsi a mbwerera komanso mphamvu za magetsi ena popanda kugwiritsa ntchito nkhuni kapena makala osavomelezeka ndi boma.
- Zimenezi zingapangitse kuti mavuto monga a njala komanso kukwera mtengo ndi kuzimazima kwa magetsi opangidwa ndi mphamvu ya madzi athe.

## Kodi mumagwiritsa ntchito mphamvu zanji pakuphika kapena kutenthetsa zinthu pa khomo panu?

Dziko likakhala ndi magetsi odalilika, ntchito za mafakitale ndi malonda zimayenda bwino komanso miyoyo ya anthu imapita patsogolo.  Kuwonjezera apo, chilengedwe monga nkhalango zimatetezeka popeza anthu sadalira kudula mitengo kuti adziotcha makala kuti apeze zosowa pa miyoyo yawo.

Dziwani kuti, ku Malawi kuno, makomo 96 mwa makomo 100 aliwonse amagwiritsa ntchito nkhuni kapena makala pophika. Kuwonjezera apo, anthu 76 mwa anthu 100 aliwonse okhala m'madera a m'tauni amagwiritsa ntchito makala pophika. Zikuwoneka kuti Amalawi sakufuna kusiya kugwiritsa ntchito nkhuni ndi makala ndipo izi zikhala chomwechi kwa zilumika zambiri. Zonsezi zikuyika pa chiopsezo nkhalango zathu.

Chomvetsa chisoni n'chakuti; ngakhale kuti mawanja 42 mwa mawanja 100 aliwonse m'mizinda ya Lilongwe, Blantyre, Zomba ndi Mzuzu amagwiritsa ntchito magetsi opangidwa ndi mphamvu za madzi powalitsa pa malo, ndi mawanja 11 okha amene amagwiritsa ntchito magetsi pa ntchito zophika kapena kutenthetsera zinthu. Izi ziri chomwechi popeza anthu ambiri m'dziko muno amaganiza kuti mtengo wa magetsi ndi okwera kwambiri. Vuto lina ndi lokuti anthu sadziwa kuti pali njira zina zamakono zophikira ndi kutenthetsera zinthu. Anthu enanso amagwiritsa ntchito makala kamba ka vuto la kuzimazima kwa magetsi.

## Nkhalango Ziri Pa Chiopsezo

Kuchuluka kwa chiwerengero cha anthu m'dziko muno kwapangitsa kuti anthu ambiri adzidalira nkhuni ndi makala pophika. Izi zaika pa chiopsezo tsogolo la mitengo komanso nkhalango m'dziko muno. Mitengo ina ikugwetsedwa m'malo amene kumachokera a kasupe, zimene zikupangitsa kuti mpweya usamatsukidwe bwino ndi mitengo popeza mpweya oyipa umene anthu amatulutsa ndi umene mitengo imagwiritsa ntchito popanga chakudya chake, ndikutulutsa kunja mpweya umene anthu timapuma. Kudula mitengo kukupangitsanso kuti malo amene madzi ndi akasupe amatuluka asamakhale achinyontho kamba kothawa kwa nthuzi opangika ndi mitengo, zimene zingapangitse madzi kumauma



mwachangu m’dziko muno. Nazo zamoyo zimene zimadalira mitengo ziri pa chiopsezo chokufa.

Tikunena pano, mitengo yokwana mahekitara zikwi makumi atatu [30,000] a nkhalango ikugwetsedwa chaka chiri chonse m’dziko muno.

Tikapanda kuchitapo kanthu, pofika chaka cha 2050, nkhalango zambiri m’dziko muno zidzakhala zitapululuka. Zimenezi zidzabweretsa mavuto pa chuma, ndikusokoneza ntchito zotukula miyoyo ya anthu.

## Zotsatira Zodula Mitengo Mosayang’ana Mawa

Munthu opanga makala amadula mtengo onse— kuphatikizapo mizu, tsinde ndi masamba— ngakhale kuti mbali zimene zimafunika pootcha makala ndi zochepa. Nayo nthaka imakokoloka mizu ya mitengo ikazulidwa, ndipo zotsatira zake zimakhala zosaneneka, kuphatikizapo izi:

- **Kukokoloka kwa nthaka:** Kudula mitengo ndi kuotcha makala mosatsatira malamulo kumapangitsa kuti nthaka ichite dazi kamba kosowa choyitchinjiriza. Zimenezi zimasokoneza ntchito yowonetsetsa kuti dziko lino likhale ndi chakudya chokwanira. Mchitidwewu umapangitsanso kuti nyengo izisintha mwachangu, ndipo umphawi umachuluka popeza anthu amasowa pogwira ntchito za ulimi zikalowa pansi.
- **Kusokonekera kwa ntchito zopanga ndi kugawa magetsi m’dziko:** Kuchepa kwa mitengo munkhalango zathu ndi madera ena kumapangitsa kuti dothi lokokoloka ndi madzi osefukira

### Mgwirizano wa pakati pa nkhalango ndi mphamvu za magetsi

**Mitengo ikachepa, mvula imachepa ndipo madzi opangira magetsi ochoka ku mphamvu za madzi amakhala operewera. Izi zimapangitsa kuti anthu azidula mitengo mwachisawawa pofuna kupeza nkhuni kapena makala ophikira.**

likafike ku mitsinje yopangira mphamvu za magetsi mosavuta ndi mwachangu, ndi kusokoneza ntchitozo. Zimenezi zimasokoneza ntchito za malonda popeza mafakitale amagwiritsa ntchito magetsi osadalirika pa ntchtio zawo. Zimenezi zimasokonezanso ntchito za malonda m'dziko popeza anthu ndi kampani sangafune kuyambitsa ntchito za malonda m'dziko limene magetsi ake ndi osadalirika.



- **Kuchuluka kwa chiwerengero cha ngozi zodza mwadzidzidzi:** Masiku ano, nkhani ya kusefukira kwa madzi iri mkamwa-mkamwa popeza mchitidwe odula mitengo mwachisawawa wapangitsa kuti madzi adziyenda mothamanga popanda mitengo yowachedwetsa kapena yowayimitsa. Kamba ka vuto la madzi osefukira, miyoyo ya anthu, zifuyo, nyama za kuthengo ndi katundu wambiri zawonongeka, zinthu zimene zikanatetezeka tikanasamala mitengo.

## Nkhani Yabwino Ndi Yokuti Tsopano Pali Njira Zambiri Zophikira Ndi Kutenthetsera Zinthu Kupatula Kugwiritsa Ntchito Nkhuni Ndi Makala

Ngakhale anthu ena amayikira kumbuyo m'chitidwe ogwiritsa ntchito nkhuni ndi makala, ati ponena kuti anthu alibe mtengo ogwira, zoona zake ndi zokuti masiku ano tadala popeza pali njira zambiri zoyatsira moto ndi kuphikira komanso kutenthetsera zinthu kapena pa malo. Tidziwe kuti si makala onse amapangidwa mosatsata malamulo, popeza boma limapereka ziphaso zopangira makala kwa anthu, mabungwe ndi makampani ovomerezeka. Choyeneranso kudziwa ndi chokuti, ngakhale si onse amagwiritsa ntchito magetsi ochokera ku mphamvu zopangidwa ndi madzi, anthu ambiri a

m'matauni ali ndi mwayi olumikizidwa ku magetsiwa.

Tikagwiritsa ntchito magetsi, gasi ndi mphamvu za magetsi a mbwerera, sipakhala utsi wambiri, zimene zimapangitsa kuti mpweya usawonongeke, ndipo nyengo siisintha mwachisawawa popeza zipangizozi sizitenthetsa moposa mulingo pa malo. Zimenezi zimapangitsa kuti anthunso apulumuke ku nthenda zokudza kamba kopuma mpweya osayenera ndi zina. Ubwino ogwiritsa ntchito njira zina kupatula makala ndi nkhuni ndi okuti munthu suwononga ndalama zambiri. Izi ndi malinga ndi kafukufuku amene wachitidwa posachedwapa.

## Kodi mukudziwa?

- Matope amapangitsa kuti ndalama zambiri zigwiritsidwe ntchito popanga magetsi oyendera mphamvu za madzi.
- Mapeto ake, ogwritsa ntchito magetsi amalipira ndalama zambiri kuti aphikire kapena kudzitenthetsera.
- Pakati pa zaka za 2016 ndi 2019, bungwe la EGENCO lachotsa matani 105,000 a matope kuchoka mu mtsinje wa Shire.

# Khalani Otsogola, Gwiritsani Ntchito Njira Zosawononga Za Chilengedwe

Tikhoza kuchita izi popanga izi:

- **Kusiya** kugwiritsa ntchito nkhuni ndi makala osavomelekeka pophika ndi kutenthetsa zinthu.
- **Tiyambe** kugwiritsa ntchito magetsi, gasi ndi makala ovomelezeka ndi boma.
- **Tiyambe** ntchito zina za malonda, kusiyana ndi zogulitsa



nkhuni ndi makala osavomelezeka.

- **Tidziwitse abale ndi anansi** za ubwino wakugwiritsa ntchito njira za makono zophikira ndi kutenthetsera zinthu kupatula makala ndi nkhuni. Mukhozanso kuwadziwitsa anzanu kuti ndikotheka kugwiritsa ntchito makala ovomelezeka ndi boma.



*Uthengawu wakonzedwa pansi pa ntchito ya Tiphike Mwa Makono Poteteza Nkhalango (Modern Cooking for Healthy Forests in Malawi") ndi chithandizo chodzera ku mabungwe a USAID ndi UKaid.*



**The Centre for Environmental Policy and Advocacy, CEPA,** is a Malawian civil society organisation that advocates for environment and natural resources policies to be implemented for sustainable development.

**Info@cepa.org.mw / www.cepa.org.mw**

USAID
KUCHOKERA KWA ANTHU AKU AMERICA

UKaid
from the British people